EXAMINATIONS COUNCIL OF ZAMBIA

Examination for School Certificate Ordinary Level

# Cinyanja 3156/1

Pepala Loyamba

## Specimen

Zina Zofunikira

Nthawi: Maola Awiri

**Malangizo Kwa Olemba Mayeso**

www.eczpastpapers.com

Lemba dzina lako, nambala ya malo komwe ulembera mayeso ndiponso nambala yako iwe amene ulemba mayeso.Ulembe izi m'malo omwe apatsidwa mukabuku kamayankho.

Pepala la mayeso ili lili ndi zigawo zitatu **A**, **B** ndi **C**.

Yankha funso limodzi kucokera pa cigawo ca **A**, yankha mafunso anai alionse kucokera mucigawo ca **B** ndipo yankha mafunso yonse amene ali mucigawo ca **C.**

Lemba mayankho ako mukabuku kamayankho komwe kapatsidwa.

Ngati wagwiritsira nchito mopitirira kabuku kamodzi, umang

mwatsatane-tsatane timabuku tonse timene wagwiritsa nchito.

Uziwerenga mobwereza-bwereza ndi kumvetsetsa malangizo omwe alembedwa pamwamba pa funso lililonse.

**Zina Zolangiza Olemba**

Nambala ya mamaliki yaikidwa mu mlungako [ ], kumatsiriziro kapena kumbali kwa funso lili lonse, mwatsatane-tsatane.

www.eczpastpapers.com

## A CIGAWO COYAMBA – CIMANGIRIZO [MAMALIKI 40]

**Musataye nthawi yopitirira ola limodzi pa cigawo coyamba.**

**Lembani cimangirizo m'Cinyanja comveka bwino pa mutu umodzi wa mitu yotsatirayi. Cimangirizo canu cikhale pakati pa mau 250 ndi 350.**

**Mitu ya nkhani**

**1** "Boma lifunika Kumanga nyumba, m'malo Osiyana – siyana, kuti lizisungiramo anthu okalamba."

Perekani maganizo anu, mobvomekeza kapena mokana, pa ganizoli.

**2** Lembani kalata kwa msuweni wanu kumupempha thandizo la ndalama zakuti mukalipire ku sukulu kwanu temu likubwerali.

**3** Fotokozani mofikapo kweni – kweni za maonekedwe a sukulu lanu.

**4** Lembani za kukoma ndi kuipa kosuta fodya wacamba.

## B CIGAWO CACIWIRI – ZA M'MABUKU [MAMALIKI 40]

**Yankhani molunjika mafunso ya m'mabuku anai cabe mwa asanu awa.**

www.eczpastpapers.com

**1 CIKONDI SAUMIRIZA** *(Jerry Banda)* **[10]**

**(a)** Verona atalandira kalata kucoka m' manja mwa m'ng'ono wake anati; "Siizotu zaululika, imani ndikuwerengereni mudzimvere nokha."

**(i)** Ndani anauzidwa mau awa? [2]

**(ii)** Chulani mlembi wa kalatali. [1]

**(iii)** Kodi uthenga unali mkalatali unali wakuti ciami? [3]

**(b)** Fotokozani zilango zimene Chale ndi A Hendriko amalandira kothera kwa nkhaniyi. [4]

**2 MATSOTSI** – *(G.H. Shonga ndi J. N. Zulu)* **[10]**

**(a)** Kodi Robato Balala anakacitira kuti chuti cake? [1]

**(b)** Chulani dziko kumene kupezeka mzinda wa Jubeki [2]

**(c)** M'bukuli muli mau awa; "Koma pepani sinditha kunena poti ndinali wotanganidwa. Comwe ndingadziwe ncakuti pamene ndinali kulemba, Bwana Menijala anandipita kumbuyo ndi mnyamata wina, ndiganiza agwira nchito mom'muno.

www.eczpastpapers.com

Mnyamatayo anapatsana moni ndi munthu amene mukunena kuti ndinali nayeyo ..."

(i) Ndani amanena mau awa? [1]

(ii) Nanga anali kuuza yani? [1]

(iii) Chulani mnyamata amene anali ndi Bwana Menimjala [1]

(iv) Nanga anapatsidwa moni ndani? [1]

(v) Kodi ndi nkhani yanji imene inali kufufudzidwa apa? [2]

(d) Kodi matsotsi anagwidwira kuti? [1]

3 **IKAKUONA LITSIRO SIKATA** *(Jolly Max Ntaba)* **[10]**

(a) M'bukuli muli mau awa;

"Iii, hee, ndinaopa kuti mucedwe, ...anatero akukhazikika bwino pa ciwofo – wofo ca mpando. Ndamunamiza Fulolesi kuti ndikupita ku chipatala, mutu ukuwawa ..."

(i) Chulani yemwe ananena mau awa [1]

(ii) Anali kuuza yani? [1]

www.eczpastpapers.com

(iii) Nanga ouzidwayo anali ndi yani? [1]

(iv) Kodi ulendoyu anali kupita kuti? [1]

(b) Kodi mukadakhala m'polisi, mukadamuimba mlandu wanji woyendetsa galimoto limene linacita ngozi? (Sankhani cabe yankho limodzi mwa awa;)

A Wonyamula anthu ali paubwenzi

B Wosasamala galu wamkupe

C Woyendetsa galimoto mosasamala [2]

(c) Mau yakuti, 'Cikondi Ciribe Maso,' angagwire nchito bwino kulingana ndi nkhani iri m'bukuli. Perekani umboni pa ...

4 **MASAUTSO A KAMNJIRA** *(Jerry N. Banda)* **[10]**

(a) Kodi ndi cifukwa ciani anthu anakhumudwa ndi imfa ya Nthandakuca? [2]

(b) M' bukuli muli mau awa; "Kodi apo muli inupo, ndithu-ndithu ndi mtima wanu wonse mwafunitsitsa kuti Mankhume akhale mwamuna wanu?



www.eczpastpapers.com

(i) Chulani amene ananena mauwa. [1]

(ii) Perekani cifukwa cimene wolankhulayo ananenera mauwa. [1]

(iii) Nanga ndani anafunsidwa funsoli? [1]

(c) Fotokozani mwatsatane –tsatane m'mene zinacitikira posankha Mfumu Nyangu watsopano. [5]

5 **MALIRO NDI MIYAMBO YA ACHEWA** – *(Archibald J. Makumbi)* **[10]**

(a) Kodi mwambo ndi ciani? [2]

(b) Perekani zifukwa zimene mkazi wodwala pakati, kawiri – kawiri, anali kuonera mwana wopanda mphamvu mwina woferatu panthawi yocira. [3]

(c) Kodi chitengwa ndi ciani? [3]

(d) Kodi ndi ana otani amene anali kugulitsidwa ndi makolo ao ngati akapolo? [2]

## C CIGAWO CACITATU – MIYAMBI NDI MIKULUWIKO [MAMALIKI 20]

**Muyenera kuyankha mafunso onse m'cigawo ici (1 ndi 2)**www.eczpastpapers.com

1 **Miyambi** **[10]**

**Perekani matanthauzo a miyambi isanu yotsatirayi:**

(a) Cimanga chilola opanda mano.

**Tanthauzo:** ........................................................................ [2]

(b) Kudza kawa mafinya ndi munga omwe.

**Tanthauzo:** ........................................................................ [2]

(c) Maso aipsa, kamwa likonza; Maso ali ndi njiru.

**Tanthauzo:** ........................................................................ [2]

(d) Mwana wa ng'ona sakulira dziwe limodzi.

**Tanthauzo:** ........................................................................ [2]

(e) Kwa eni kulibe mkuwe.

**Tanthauzo:** ........................................................................ [2]


www.eczpastpapers.com

**2 Mikuluwiko** **[10]**

**Perekani matanthauzo a mikuluwiko isanu yotsatirayi. Kenaka muigwiritsire nchito m'ziganizo za m'Cinyanja comveka bwino kusonyeza kuti mukuidziwadi.**

**Citsanzo:** Kanjipiti

**Tauthauzo:** Munthu wamfupi.

**Ciganizo:** Zimbani anakwatira Kanjipiti.

**(a)** Dooka nkhali:

**Tanthauzo:** ........................................................................ [1]

**Ciganizo:** ........................................................................ [1]

**(b)** Myenda nazo:

**Tanthauzo:**........................................................................ [1]

**Ciganizo:** ........................................................................ [1]

**(c)** Kadam'manja:

**Tanthauzo:**........................................................................ [1]

www.eczpastpapers.com

**Ciganizo:** ........................................................................ [1]

**(d)** Caka – cadza :

**Tanthauzo:**........................................................................ [1]

**Ciganizo:** ........................................................................ [1]

**(e)** Dzuwa liwamba mtengo:

**Tanthauzo:**........................................................................ [1]

**Ciganizo:** ........................................................................ [1]

**Mayeso Anu Atha**



www.eczpastpapers.com